# Malongosoledwe a coonadi ca m’Baibulo

## Za Mulungu wamkulu

1. Mulungu ndi m’modzi
2. Mulungu ali paliponse
3. Mulungu adziwa zonse
4. Mulungu ndiye Atatu
5. Mulungu ndi woyera
6. Mulungu ndi wamphamvu zonse
7. Mulungu ndi wokhulupirika
8. Mulungu ali ndi maina ambiri

# 1. Mulungu ndi m'modzi

*Yehova ndiye Mulungu, m'thambo la kumwamba ndi pa dziko lapansi; palibe wina – Deuteronomo 4.39b*

**Kuwerenga**
Deuteronomo 6.4-7

**Malongosoledwe**
Mwina nthawi zina munalakalaka kukhala monga mbalame wouluka. Mwina munalakalaka kukhala ndi mapiko kuti mungauluke kumwamba kukaona nyenyezi zonse. Ngakhale mukauluka masiku ambiri simudzakwaniritsa kuona nyenyezi zonse, cifukwa kuli nyenyezi zambiri! Kuli zikwi ndi zikwi!
Mulungu analenga nyenyezi zonse. Analenga nyenyezi iriyonse. Ndipo analenga zinthu zina zonse zimene tiona.
Kale kale Aisrayeli anali anthu a Mulungu. Kunali anthu ambiri pa dziko lapansi, koma Mulungu anasankha Aisrayeli kukhala anthu ake apadera. Mulungu analankhula nao kupyolera mwa Mose. Anawapatsa dziko lokongola kuti Aisrayeli akhalemo. Anawauza kuti kuli Mulungu m'modzi: Iye yekha. Kulibe milungu ina, ndiye Aisrayeli sanayenere kubembedza wina aliyense koma Iye yekha.
Anthu amene anakhala m'maiko ozungulira dziko la Israyeli, anaganiza kuti kuli milungu yambiri: mulungu m'modzi amene adapanga nyenyezi, wina amene adapanga mwezi ndi wina amene anakhala m'nyanja. Anthuwo anapanga mafano ao mogwiritsa nchito mitengo ndi miyala.
Nthawi zina anthu a Mulungu anaiwala za Iye napanga mafano kuwapembedza. Anaiwala angakhale anadziwa kuti Mulungu ndi wabwino ndi wosangalatsa.
Tsiku lina Mulungu anatuma mneneri Yesaya kuuza Aisrayeli kuti ndiwo opusa kwambiri. Mneneri Yesaya ananena, 'Mverani. Ndidzakufotokozani kuti ndinu opusa kwambiri. Mwamuna wonyamula nkhwangwa angapite ku nkhalango. Atapeza mtengo wabwino audula. Auwaza. Apanga moto mogwiritsa nchito zidutswa zina za mtengo. Atatsiriza kupanga moto akamba kuti, 'Ha, moto uwu ndi wabwino ndi wotentha'. Kenaka atenga cidutswa cina za mtengowo napita kunyumba. Acidula ndi kusema ndipo acipangitsa kuoneka monga munthu wokhala ndi makutu, maso, mphuno ndi kamwa. Kenaka aikapo golide lowala. Ndipo anena, 'Onani. Ndapanga mulungu wanga!' Apembedza cidutswa ico ca mtengo. Iye ndiye munthu wopusa kwambiri! Cidutswa ico ca mtengo sicikhoza kumva. Sikhoza kuona. Sicikhoza kuyenda. Cidutswaco ndi fano. Sicinalenge dziko lapansi ndi thambo. Sicinalenge nyenyezi. Sicinapatse mvula.'
Mneneri Yesaya anati kuti kuli Mulungu woona m'modzi cabe. Iye analenga zonse. Iye yekha ndiye Mbuye wa zonse. Zonse ziri zake. Iye amasamalira zonse.
Sitikhoza kuona Mulungu cifukwa Iye ndiye Mzimu. Koma Iye ndiye Mulungu amene atimva pamene tipemphera. Iye ndiye wamkulu kwambiri.

**Kukambirana**
1. Fano ndi lirilonse pa limene timadalirapo kuposa Mulungu, mwacitsanzo ndalama, nzeru, cithumwa kapena mankhwala. Kodi muli mafano m'umoyo wanu?
2. Ndi cifukwa ciani ndife opusa ngati tipanga mafano?
3. Ndi cifukwa ciani Mulungu ndiye Mwini wa zonse?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Inu ndinu Mulungu woona. Mutipatse mtima wosadalira pa wina aliyense koma pa Inu nokha. Tidziwa kuti mutimva pamene tipemphera, cifukwa Inu ndinu wamkulu kwambiri. M'dzina la Yesu tikupemphani izi. Amen.

## 2. Mulungu ali paliponse

*Kodi Ine sindidzala kumwamba ndi dziko lapansi? ati Yehova – Yeremiya 23.24b*

**Kuwerenga**
Salimo 95.1-6

**Malongosoledwe**
Mulungu ali paliponse!
Pamene tipenya uku ndi uku sitikhoza kuona Mulungu. Koma ali pano ndiponso uko. Ali pafupi nafe ndiponso kutali Kumwamba. Ndiponso ali kutali ku mbali ina ya dziko lapansi.
Mulungu akhala paliponse pa nthawi imodzi cifukwa Iye ndiye Mulungu ndiponso Mzimu. Mulungu ndi wamkulu kwambiri.
Baibulo litiuza za mkazi wacicepere wochedwa Haga. Haga anali mdzakazi. Sara, mkazi wa Abrahamu, anali bosi wake. Tsiku lina Haga anathawa kucokera kwa Sara, cifukwa Sara adamcitira coipa. Haga anapita kutali ku dziko la cilendo. Anaganiza kuti palibe womkonda iye. Anali wosakondwa kwambiri. Akhala pansi pafupi ndi citsime ca madzi. Ndipo anaganiza kuti anali yekha.
Koma sanali yekha. Mulungu analipo. Anamuona. Anadziwa zobvuta zake. Anadziwa kuti mtima wake unali wacisoni kwambiri. Ndipo Iye anamkonda.
Mwadzidzidzi Haga anamva Mulungu polankhula naye. Mulungu anati, Haga, bwerera kwa Sara. Cita zimene adzakuuza kucita. Ndidzakusamalira.'
Haga anadabwa. Anati, 'Sindinaganizire kuti Mulungu andiona pano! Koma andiona ndithu!'
Haga anakondwera. Anamvera Mulungu. Anabwerera kwa Sara ndipo Mulungu anamsamalira.
Haga anakondwa kwambiri podziwa kuti Mulungu anamuona. Adali wacisoni ndipo adaganiza kuti anali yekha. Koma Mulungu ankamuona nthawi zonse.
Kuzindikira kuti Mulungu ali paliponso, kuti ationa ndipo kuti sitiri tokha nthawi zonse kufunika kutipangitsa kukhala okondwa kwambiri.
Usiku pamene muli pa bedi kukagona Mulungu alipo. M'cipinda mungakhale mdima koma simuyenera kucita mantha. Pamene muli nokha popita ku sukulu simuli cabe nokha ndithu. Mulungu alipo. Ali pafupi nanu. Kodi kudziwa kuti Mulungu ali paliponse ndiko cinthu cakukondweretsani?
Kudziwa kuti Mulungu ali paliponse kutipangitsanso kukhala ocenjera.
Pamene muli kusewera Mulungu alipo. Aona zimene muli kucita. Akumva zimene mukamba. Ngati tikumbuka izi tikhala ocenjera polankhula ndipo ticita cabe zimene zikondweretsa Mulungu.
Kudziwa kuti Mulungu ali paliponse kutidabwitsa.
Ife tikhoza kukhala pa malo amodzi cabe nthawi imodzi. Pa nthawi yomwe muli kunyumba simuli ku sukulu. Ngati muli mkati simuli pabwalo. Koma Mulungu ali ponseponse. Yang'anani thambo la kumwamba. Yang'anani nyenyezi. Yang'anani mozungulira mwanu monsemo. Ganizirani, 'Mulungu ali paliponse! Paliponse!' Mulungu ndi wodabwitsa kwambiri!

**Kukambirana**
1. Kodi ndi cotheka bwanji kuti Mulungu ali paliponse?
2. Ndi cifukwa ciani tiyenera kukhala okondwa podziwa kuti Mulungu ali ponseponse?
3. Ndi cifukwa ciani tiyenera kukhala ocenjera podziwa kuti Mulungu ali ponseponse?
4. Ndi yani amene anaganiza kuti Mulungu sanamuone kodi?
5. Ndi cifukwa ciani tifunika kudzicepetsa poganiza kuti Mulungu ali ponseponse?
6. Kodi mukumva bwanji poganiza kuti Mulungu ali paliponse?

**Citsanzo ca pemphero:**
Mulungu wamkulu, Pamene tipemphera tidziwa kuti muli pafupi nafe. Muli paliponse. Sitimvetsa kuti mumakhala paliponse. Mutithandize kukumbukira kuti mukhala pafupi nthawi zonse kuti tizicita zimene zikukondweretsani nthawi zonse. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu Mpulumutsi. Amen.

## 3. Mulungu adziwa zonse

*Inu mudziwa kukhala kwanga ndi kuuka kwanga – Salimo 139.2a*

**Kuwerenga**
Salimo 139.1-10

**Malongosoledwe**
Anyamata ndi atsikana atakula amapita ku sukulu. Amapita ku sukulu kuphunzira. Kuli zambiri zimene tingaphunzire.
Koma Mulungu sapita ku sukulu. Iye sayenera kuphunzira. Mulungu adziwa zonse.
Mulungu adziwa zinthu zimene ife sitidziwa. Adziwa ziwerengero za nyenyezi kumwamba. Acha nyenyezi zonse kumwamba maina zao.
Mulungu adziwa zimene sitikhoza kuona. Adziwa m'mene mizu ya mitengo yaikulu imakula m'nthaka ndiponso m'mene mizu imatumizira madzi ku timasamba ting'ono-ting'ono.
Mulungu adziwa zonse zimene zicitika m'mdima. Kulibe munthu amene angabise kwa Iye, ngakhale kuli mdima waukulu wa usiku.
Mulungu adziwanso zimene ziri m'mitima yathu. Adziwa zimene tiganiza. Adziwa cinsinsi ciriconse. Mulungu adziwa zonse.
Baibulo litiuza za mfumu yaikulu: Nebukadinezara. Usiku wina mfumu Nebukadinezara analota loto lodabwitsa. Atauka sanakhoze kulikumbikira. Sanakondwere pa ico.
Mfumu anaitana anthu ake ocenjera. Anawauza, 'Ndiuzeni loto langa!' Koma iwo analephera kuuza loto lake. Kodi iwo angadziwe bwanji loto la mfumu? Mfumu anakalipa.
Danieli anali m'modzi wa anthu ocenjera a mfumu. Danieli anati, 'Ndidzapempha Mulungu kundiuza loto la mfumu'.
Danieli ananena, 'Mulungu adziwa zinthu zonse zobisika. Adziwa zimene ziri m'mdima. Adziwanso maloto athu.'
Danieli anapemphera ndipo Mulungu anamuuza loto la mfumu. Mulungu analidziwa kale nthawi zonse. Ndipo kenaka Danieli anauza lotolo kwa mfumu.
Mulungu adziwanso zinthu zimene zidzacitika m'tsogolo. Timapanga maganizo. Tingakambe, 'M'mawa ndidzapita kusewera', kapena 'M'mawa ndidzapita ku sukulu'. Koma sitidziwa zimene zidzacitika tsiku ikudzayo. Ndi Mulungu cabe amene adziwa zimene zidzacitika mawa, mazo ndi caka ca m'mawa.
Mulungu ndiye wamkulu kwambiri. Adziwa zonse.

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani Mulungu sayenera kuphunzira?
2. Kodi Mulungu adziwa zimene ticita mdima?
3. Kodi Mulungu adziwa zimene tiganiza?
4. Kodi Mulungu adziwa zimene zidzacitika m'tsogolo?
5. Kodi mukumva bwino kuti Mulungu adziwa zonse za inu?
6. Mulungu adziwa macimo omwe ali m'mitima yathu. Ndi cifukwa ciani tifunika Yesu kutiyeretsa ku mitima yathu yocimwa?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Mudziwa zonse. Mudziwa zonse za miyoyo yathu ndi mitima yathu. Mudziwa macimo athu ndiponso kuti sitikwaniritsa kudziyeretsa ku macimo athu. Tifunika Mwana wanu Yesu Kristu, Mpulumutsi kuti atiyeretsa ku uchimo. Mudziwanso ngati tilakalaka kukulondolani moonadi. Inu ndinu wamkulu ndi wodabwitsa! M'dzina la Yesu tikupemphani izi. Amen.

## 4. Mulungu ndiye Atatu

*Yehova ndi wamkulu, nayenera kulemekezedwa kwakukulu – Salimo 145.3a*

**Kuwerenga**
Mateyu 28.16-20

**Malongosoledwe**
Mulungu ndi wamkulu kwambiri kotero kuti sitikhoza kudziwa zonse za Iye. Sitikhoza kumvetsa Mulungu.
Baibulo likamba kuti Mulungu ndiye m'modzi. Tinaphunzira kale kuti kuli cabe Mulungu m'modzi. Koma Baibulo litiuzanso kuti Mulungu ndiye Atatu. Mulungu ndiye Atatu komabe ndiye m'modzi. Ici ndi cinthu cimene sitikhoza kumvetsa.
Baibulo litiuza za Mulungu Atate, Mulungu Mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera. Iwo ndiwo Atatu.
Mulungu Atate ali Kumwamba. Yesu ndiye Mulungu Mwana. Yesu anadza pa dziko lapansi monga Mwana wakhanda. Timakumbukira kubadwa kwake pa tsiku la Krisimasi. Mulungu Mzimu Woyera anatsika kocokera Kumwamba kukhala ndi Yesu. Anadza pamene Yesu anabatizidwa. Ndipo anadzanso kukhala m'mitima ya anthu okhulupirira Yesu.
Kunali mwamuna wochedwa Yohane amene anabatiza anthu m'mtsinje. Anthu anamcha Yohane Mbatizi. Yesu anafuna kubatizidwa.
Yohane ndi Yesu anapita m'madzi pamodzi. Yohane anabatiza Yesu. Pamene anacoka m'madzi Yohane anaona cinthu codabwitsa. Cinthu cooneka ngati nkhunda cinatsika kucokera Kumwamba. Cinadza naima pa mutu wa Yesu.
Ico sicinali nkhunda yoona. Cinali Mulungu Mzimu Woyera m'cifaniziro ca nkhunda. Pa nthawi imeneyo Yohane anamva mau. Mau anati, 'Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa'. Mau awa analankhulidwa ndi Mulungu Atate. Iye analankhula kucokera Kumwamba.
M'njira iyi Mulungu anadzionetsa kukhala Atatu. Yesu (Mulungu Mwana) anabatizidwa. Mulungu Mzimu Woyera anadza m'cifaniziro ca nkhunda. Mulungu Atate analankhula kucokera Kumwamba. Mulungu ndi wodabwitsa ndi wamkulu kwambiri!
Masiku ano timabatiza anthu m'dzina la Mulungu Atate, Mulungu Mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera, pakuti Mulungu ndiye Atatu.

**Kukambirana**
1. Kuli Mulungu m'modzi cabe. Ndi cifukwa ciani tikambanso kuti Mulungu ndiye Atatu?
2. Kodi Mulungu Mwana ndiye yani?
3. Kodi Mulungu Mzimu Woyera anaonekera bwanji atabatizidwa Yesu?
4. Kodi ndi yani amene analankhula mau kucokera Kumwamba pa nthawi ya cibatizo ca Yesu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Atate tikuyamikani pakuti ndinu wamkulu ndi wabwino kwambiri. Mulungu Mwana tikuyamikani pakuti munabwera pa dziko lapansi kupulumutsa anthu ocimwa. Mulungu Mzimu Woyera tikuyamikani kuti mupangitsa anthu kukhala ana a Mulungu. Sitimvetsa kuti ndinu m'modzi komanso Atatu. Nzeru zathu ndi zazing'ono. Mutithandize kuphunzira zina zambiri za Inu. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu Mpulumutsi. Amen.

## 5. Mulungu ndi woyera

*Woyera, Woyera, Woyera, Yehova wa makamu; dziko lonse lapansi ladzala ulemerero wace – Yesaya 6.3*

**Kuwerenga**
Salimo 99

**Malongosoledwe**
Yesaya anali m'modzi wa aneneri akulu a Mulungu. Mulungu analankhula ndi mneneri Yesaya nthawi zambiri. Analangiza mneneri Yesaya kuuza anthu a Mulungu kuti tsiku lina kudzakhala Mpulumutsi wodabwitsa.
Tsiku lina Mulungu analankhula ndi mneneri Yesaya m'masomphenya. Masomphenya ndi monga loto. M'masomphenya mneneri Yesaya anaona Ambuye kukhala pa mpando wacifumu wautali. Zobvala za Mulungu zinadzala m'Kacisi. Pamwamba pa Iye panali aserafi. Aserafi ndiwo zolengedwa zowala za m'Mwamba.
Mneneri Yesaya anaona kuti serafi aliyense anali ndi mapiko asanu ndi limodzi. Aliyense anagwiritsa nchito mapiko ake awiri kuphimba nkhope yake, mapiko ena awiri kuphimba mapazi ake ndipo mapiko awiri anauluka nao.
Aserafi anapfuula kwa anzao. Wina anati, 'Woyera, Woyera, Woyera, Yehova wa makamu; dziko lonse lapansi ladzala ulemerero wace'. Kenaka wina anayankha, 'Woyera, Woyera, Woyera'.
Mneneri Yesaya anamva mantha poona masomphenya awa. Masomphenya anamuonetsa kuti Mulungu ndiye woyera.
Kodi ici citanthauza ciani?
Kodi Baibulo litanthauza ciani pamene litiuza kuti Mulungu ndiye woyera?
Kodi mukumbukira nthano ya Mose kuti Mulungu anamuonetsa ulemerero wake pang'ono kotero kuti nkhope ya Mose inawala monga dzuwa? Kuwala uko kunali mbali ya ciyero ca Mulungu.
Koma ciyero ca Mulungu ndi cacikulu cuposa kuwala cabe. Mulungu ndiye wopanda uchimo. Mulungu sacimwa nthawi zonse. Mulungu amacita zolungama nthawi zonse. Iye ndiye kuwala ndi ulemerero ndithu. Iye ndiye ubwinodi. Kulibe kanthu kocimwa komwe kangabwere pafupi naye cifukwa kanthuko kadzatenthedwa ndi ciyero ca Mulungu.
O, ciyero ca Mulungu ndi cacikulu kwambiri. Angelo ndi aserafi aciona ndipo amalemekeza Mulungu usana ndi usiku. Amamuimbira ndi kumtumikira. Angelo ndiwonso oyera. Sacimwa. Koma Mulungu ndiye woyera kwambiri kuposa angelo. Cifukwa cake aserafi anaphimba nkhope zao ndi mapazi ao. Cifukwa cake amakamba kuti Iye ndiye Mulungu wa makamu.
Ngati kanthu kocimwa kalikonse sikangapite kwa Mulungu, ife tingapite bwanji kwa Iye kodi? Pamene tiganizirako kuti ndife ocimwa ndipo kuti Mulungu ndiye wamkulu ndi woyera kwambiri sitilimba mitima kupita naye. Sitilimba mitima kupemphera ngati tiona ciyero cake.
Koma Mulungu afuna kuti tipita kwa Iye. O, Iye aticitira zabwino! Anauza Yesaya kuti sayenera kumva mantha. Atiuzanso kuti sitiyenera kumva mantha. Koma atiuzanso m'Baibulo kuti tingapite kwa Iye m'dzina la Yesu cabe. Yesu ndi woyera. Yesu ndiyenso Mulungu. Yesu anatenga ana ang'ono m'mikono yake, ngakhale iwo anali ang'ono ndi ocimwa. Anafuna kuwabweretsanso kwa Mulungu Atate. Ndipo lero tikhoza kupita kwa Mulungu ngati tipita m'dzina la Yesu, pakuti Yesu anafa kukhululukira ndi kuyeretsa anthu ake ku macimo ao. Cifukwa ca Yesu Mulungu alola anthu kubwera pafupi naye angakhale ndiye woyera.

**Kukambirana**
1. Kutanthauzanji kuti Mulungu ndiye woyera kodi?
2. Kodi ciyero ca Mulungu citanthauza ciani kwa inu?
3. Kodi anthu ocimwa akhoza kupita bwanji kwa Mulungu Woyera?
4. Ndi cifukwa ciani timapemphera m'dzina la Yesu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Angelo akulemekezani masiku onse cifukwa ca ciyero canu. Mulibe chimo lirilonse kapena colakwa ciriconse. Zikomo kwambiri kuti munapanga njira yopulumutsiramo anthu ocimwa: Yesu Kristu. Mutithandize kukhala miyoyo yathu yoyera ndi kutsutsa uchimo wonse. Mutiyeretse kotero kuti titamwalira mudzatilola kukhala Kumwamba kuona ndi kulemekeza ciyero canu.

## 6. Mulungu ndi wamphamvu zonse

*Ndi okhala pa dziko lapansi onse ayesedwa acabe – Danieli 4.35a*

**Kuwerenga**
Danieli 4.34 ndi 35

**Malongosoledwe**
Mafumu a nthawi zakale anali ndi mphamvu. Analamulira anthu. Anthu onse anayenera kumvera mfumu wao. Iwo amene sanamvere anapatsidwa cilango.
Mfumu Nebukadinezara anali mfumu yamphamvu. Anali ndi akapolo ambiri. Ankauza akapolo zimene anayenera kucita ndipo iwo ankamumvera nthawi zonse. Ndiponso mfumu Nebukadinezara anali ndi gulu lalikulu la asirikali. Asirikali ake anali olimbika mtima ndi amphamvu. Anapita kulikonse komwe anatumidwa.
Mfumu Nebukadinezara anatuma asirikali ake ku maiko ena kuti maikowo akhalanso olamuliridwa ndi iye. Mfumu Nebukadinezara anali mfumu yaikulu.
Tsiku lina mfumu Nebukadinezara anamanga mzinda wokongola. Anaucha Babulo. M'Babulo munali nyumba zabwino ndi minda yabwino. Mzinda wa Babulo unali wokongola woposa mizinda yonse ya kale.
Tsiku lina mfumu Nebukadinezara anayenda m'nyumba yake yacifumu. Anali wodzitamandira ndi wokondwera. Anayang'anira zokongola zonse za ku Babulo ndipo anati, 'Ndine mfumu yaikulu kwambiri. Ine ndinapanga mzinda uwu wokongola. Mphamvu zanga zandipatsa ufumu waukulu.'
Koma mwadzidzidzi anamva mau ocokera Kumwamba. Mauwo anati, 'O mfumu Nebukadinezara, ufumu wako wacoka. Wacoka kwa iwe. Akapolo ako adzakucotsa m'nyumba yacifumu. Udzayamba kukhala kuthengo monga nyama…'
Ndipo ici cinacitika. Mfumu yaikulu Nebukadinezara anapitikitsidwa m'nyumba yacifumu yake. Nthawi yaitali anakhala m'thengo monga munthu wamthengo.
Koma tsiku lina pamene mfumu Nebukadinezara anali kuyenda m'thengo, iye anapenya kumwamba naganiza za Mulungu. Anayamba kulemekeza Mulungu. Anati, Mulungu ndiye Mfumu ya zinthu zonse. Amacita cifuniro cake Kumwamba ndi pa dziko lapansi.' Pothera mfumu Nebukadinezara anadziwa kuti iye anali wamng'ono ndipo Mulungu ndi wamkulu.
Kenaka Mulungu anapatsanso mfumu Nebukadinezara ufumu wake.
Mfumu Nebukadinezara anali mfumu yaikulu ndi yamphamvu. Koma anali wamng'ono ku mbali ya Mulungu. Mulungu ndi wamphamvu zonse. Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi: analankhula cabe mau ndipo kunacitika. Ndipo Mulungu amalamulira zonse. Amalondolera ndi kulamulira mafumu onse ndi ufumu wonse. Amalamuliranso kumwamba. Iye ndiye Mfumu ya zinthu zonse ndi anthu onse. Ife tiri cabe zilengedwe zake zazing'ono-zazing'ono.
Pothera mfumu Nebukadinezara anaphunzira ici ndipo anati, 'Ndi okhala pa dziko lapansi onse ayesedwa acabe' (Danieli 4.35).
Ngati tifanizira anthu ndi Mulungu wamphamvu ndi wamkulu tidzaona kuti tiri acabe.

**Kukambirana**
1. Kodi ndi yani amene anapangitsa mfumu Nebukadinezara kukhala mfumu yaikulu?
2. Ndi cifukwa ciani kudzikweza ndi chimo?
3. Patsani zitsanzo zitatu za njira momwe tingadzikweze.
4. Ndi cifukwa ciani Mulungu anacepetsa mfumu Nebukadinezara?
5. Ndi cifukwa ciani Mulungu anampatsanso mfumu Nebukadinezara ufumu wake?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Wamphamvuyonse, Mukwaniritsa kucita kalikonse komwe mufuna. Munalenga zonse ndipo mumasamalira zonse. Mutikumbutse kuti ndife anthu ang'ono ocimwa. M'mabvuto athu onse mutionetse mphamvu yanu. Nthawi zambiri tisowa cilakolako kapena mphamvu yotsutsa uchimo. Koma tidziwa kuti Yesu anagonjetsa uchimo, Satana ndi imfa pamene anafa pa mtanda. Tikuyamikani cifukwa ca mphamvu yanu. M'dzina la Yesu tikupemphani izi zonse. Amen.

# 7. Mulungu ndi wokhulupirika

*Pakuti wolonjezayo ali wokhulupirika – Ahebri 10.23b*

**Kuwerenga**
Yoswa 21.43-45

**Malongosoledwe**
Kodi mumapanga malonjezo? Ndipo mumacita zimene mulonjeza nthawi zonse kodi? Mwina munalonjeza amai anu kuti mudzacita zabwino. Koma kucita zabwino nthawi zonse ndiko kobvuta kwambiri. Ngati simucita zabwino, muphwanya lonjezo lanu.
Nthawi zambiri anthu amaphwanya malonjezo ao. Nthawi zina amaiwala. Nthawi zina amapanga lonjezo lomwe sakwaniritsa kusunga.
Mulungu saphwanya lonjezo lirilonse. Mulungu salonjeza malonjezo omwe sakwaniritsa kucita. Ndiponso saiwala malonjezo ake. Malonjezo a Mulungu ali oona. Mulungu ndi wokhulupirika.
Baibulo likamba kuti Mulungu analonjeza Aisrayeli (anthu ake a nthawi yakale) kuti adzawatsogolera ku dziko latsopano. Dziko ilo linali lokongola ndi lodzala ndi nyumba, minda, madimba, malo osungiramo nyama ndiponso zipatso zambiri zokoma.
Koma dzikolo linali kutali. Linali kutali ku tsidya lina la cipululu couma. Ndiponso kunali adani: anthu amene sanafune Aisrayeli kukhala m'dziko ilo. Iwo anatuma asirikali kumenyana ndi Aisrayeli.
Cinaoneka monga Mulungu sanakhoze kucita cimene adalonjeza!
Koma Mulungu anasamalira anthu ake m'cipululu. Anawapatsa zakudya zambiri, anawaonetsa njira ndipo anawathandiza pamene Aisrayeli anayenera kumenyana ndi adani. Pothera Aisrayeli anali pafupi pa dziko ilo. Anaona dziko ku tsidya lina kwa nyanja ya Yordani.
Koma nyanjayo inali yaikulu ndi yakuya. Ndipo kunalibe ulalo. Ana akhanda ndi anthu ena ambiri sanakhoze kusambira. Ndiponso tiana ta nkhosa sitinakhoze kusambiri. Oo, pepani! Cinaoneka monga Aisrayeli sangafike ku dziko la malonjezano. Kunalibe njira yopangira bwato ya anthu onse.
Mtsogoleri wao Yoswa anati kwa anthu, 'Konzekani kukapita ku tsidya lina la nyanja. Mulungu adzasunga lonjezo lake m'njira yodabwitsa.'
M'mawa iwo anakhala okonzeka. Yoswa anauza ansembe kupita poyamba. Iwo ananyamula Likasa. Likasa linali bokosi labwino lophimbidwa ndi golide. Ilo linali cizindikiro kuti Mulungu anali pafupi ndi anthu ake.
Ansembe anayambapo. Posacedwa anafika ku madzi. Analowamo ndipo pa nthawi imeneyo nyanja inaleka. Madzi anathamangira ku mbali ina kuli ansembe. Ku mbali ina ya nyanja madzi anaima. Mulungu sanalole madzi kuyenda kumene ansembe anaima. Ndipo posacedwa malo omwe ansembe anakhalapo anali ouma. Kunali njira youma pamene padali nyanja.
Ansembe anayenda pang'ono pa njira. Anaima pakati pa njira. Analola anthu onse kupitirira ansembe. Pamene anthu anali ku tsidya lina la nyanja ansembe anapitirizanso.
M'njira iyo Mulungu anatsogolera anthu ake onse ku tsidya lina la nyanja. Ndipo ndi ciani cimene cinacitika kodi? Anthu anapenya kumbuyo naona kuti madzi anayendanso. Nyanja inalinso yaikulu ndi yakuya. Mulungu anasunga lonjezo lake! Anawabweretsa ku dziko latsopano kumene kunali minda, madimba ndi malo osungiramo nyama. Anatenga dzikolo kucokera kwa anthu ocita zoipa nalipatsa kwa anthu omkonda.

**Kukambirana**
1. Kodi Mulungu analonjeza ciani anthu ake?
2. Kutanthauzanji kuti Mulungu ndi wokhulupirika kodi?
3. Kodi mumasunga malonjezo anu?
4. M'Baibulo muli malonjezo ambiri a Mulungu. Lonjezo limodzi ndi iri: 'Yang'anani kwa Ine, mupulumutsidwe, inu malekezero onse a dziko; pakuti Ine ndine Mulungu, palibe wina' (Yesaya 55.6). Fotokozani citanthauzo ca lonjezoli.

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wokhulupirika, Nthawi zonse mucita zimene mulonjeza. Tikuyamikani kuti simulephera kucita kalikonse komwe mufuna. Nthawi zambiri tilephera kucita zimene tinalonjeza. Mutithandize kukhala okhulupirika m'zonse zimene ticita. Tidziwa kuti mucita zimene zolembedwa m'Baibulo. Mutipatse mitima yokhulupiriradi Mau anu. M'dzina la Yesu Kristu, Amen.

## 8. Mulungu ali ndi maina ambiri

*Lilemekezedwe dzina la Mulungu ku nthawi za nthawi – Danieli 1.20b*

**Kuwerenga**
Eksodo 3.1-4 ndi 10-14

**Malongosoledwe**
Munthu aliyense ali ndi dzina lake. Ine ndiri ndi dzina. Inunso muli ndi dzina.
Ngati munthu wina akufunsani, 'Ndinu yani?' mumyankha ponena dzina lanu. Dzina lanu liuza kuti ndinu yani.
Amai anu acha dzina lanu pamene akuitanani, pamene alankhula ndi inu ndiponso pamene alankhula za inu. Dzina lanu litanthauza inu nomwe. Ngati mai aitana Belita, Yosefe sayenera kuyankha. Ngati mai aitana Yosefe, Belita sayenera kuyankha.
Dzina la Mulungu litiuza kuti Mulungu ndiye yani.
Koma Mulungu ali ndi maina ambiri. Nthawi zina timcha, 'Atate wa Kumwamba'. Nthawi zina tinena, 'Wamphamvuyonse'. Nthawi zina pamene tipemphera tikamba kuti, 'Yesu' kapena 'Ambuye'.
Baibulo litiuza za dzina lapadera kwambiri la Mulungu.
Kale kale Mulungu analankhula ndi mwamuna wochedwa Mose. Mose anafuna kuthandiza anthu ake cifukwa iwo anabvutika m'Aigupto. Koma Farao, mfumu wa Aigupto, anakalipa kwambiri kotero kuti Mose anayenera kuthawa. Tsiku lina pamene Mose anali kuweta nkhosa iye anaona citsamba ciri kuyaka moto. Citsamba cinayaka moto koma sicinanyeke. Mose anapitapo kukaona kuti ndi cifukwa ciani citsamba sicinanyeke. Ndipo pa nthawi imeneyo Mulungu analankhula ndi Mose mwa citsamba.
Mulungu anauza Mose kuti iye ayenera kupita ku Aigupto kukathandiza anthu a Mulungu. Anamuuza, 'Pitani kukabweretsa anthu anga mwa Aigupto'.
Koma Mose anamva mantha kubwerera ku Aigupto. Anamva mantha cifukwa ca Farao. Anati, 'Kodi ndinganene ciani pamene iwo andifunsa kuti ndi yani amene ananditumа?'
Mulungu anati kwa Mose, 'Auzeni kuti INE NDINE anakutumani'. Mulungu anati, 'Dzina langa ndine INE NDINE'.
Dzina ilo la Mulungu ndi lodabwitsa, iai?
Dzina ilo litifotokoza zoonadi zodabwitsa za Mulungu. Dzina INE NDINE litanthauza kuti 'Ine ndiribe ciyambi; ndinaliko nthawi zonse; sindidzasintha; ndidzakhala amodzimodzi nthawi zonse'. Dzina INE NDINE litiuza kuti Mulungu ndiye wamuyaya, kuti Iye ndiye amodzimodzi nthawi zonse, wokhulupirika, wosasintha ndiponso kuti amacita zimene alonjeza.
Dzina la Mulungu lodabwitsa koposa ndilo 'Yesu'. Dzinalo ndilo dzina loposa maina ena onse. Baibulo likamba kuti tsiku lina mabondo onse adzagwadira dzina la Yesu. Dzina lino litiuza kuti Iye ndiye Mpulumutsi.
Lamulo la Mulungu litiuza kuti tigwiritsa nchito maina a Mulungu mosamalira. Tiloledwa cabe kunena maina ake pamene tilankhula ndi Iye kapena pamene tilankhula za Iye. Maina a Mulungu ndi oyera, pakuti Mulungu ndi woyera.

**Mafunso**
1. Ndi cifukwa ciani Mose anamva mantha kuthandiza anthu a Mulungu?
2. Kodi dzina la Mulungu anamthandiza bwanji Mose kuti sanamve mantha?
3. Ndi cifukwa ciani dzina la Yesu ndi dzina labwino loposa?
4. Chulani maina ena a Mulungu.
5. Kodi tingalemekeze bwanji maina la Mulungu?
6. Patsani zitsanso zitatu m'mene tinganyoza maina a Mulungu.

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu, Atate wa Kumwamba, Zikomo kwambiri kuti mutilola kucha maina anu. Maina anu onse atiphunzitsa za Inu. Mutithandize kulemekeza dzina lanu loyera. M'dzina la Yesu tikupemphani izi. Amen.

Zolembedwa zina za m'bukuli zinasandulidwa kucokera mu buku la 'Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.'

© Stephanos Zambia Trust
www.kudziwazamulungu.com